Focus Group Discussion Guide with Community Peer Groups

Opening statements:

Zikomo povomera kutenga nawo mbali pa zokambilana izi lero.Zokambilanazi, zitenga pafupifupi ola ndi theka ndipo tikhala tikuwunika mchitidwe komanso kuthekera kwamunthu kuziyeza yekha kuti adziwe ngati ali ndi HIV mu Malawi.

Thank you for agreeing to take part in this discussion group today. The discussion will probably take about one and a half hours and we will be exploring the practice and potential for self-testing for HIV in the context of Malawi.

A. Current HIV testing services

1. **Kodi pali mitundu ingati yoyezera HIV mu dera lanu yomwe mukuyidziwa?**
   What current options for HIV testing are you aware of in your community?
2. **Kodi njira zimenezi anthu a mu dera lanu amaziwona bwanji?**
   How are these HIV testing options viewed in the community?
   - ***Kambiranani mwachidule/chindunji: ubwino komanso kuipa kwa njira zimene zatchulidwa. Mukambe pazinthu izi: Malo/dera, transport, ubwino/kuipa kwa anthu ogwira ntchito komanso m'mene amathandizira anthu, mtengo wa chithandizo, kuthekera kosintha m'mene chithandinzo chikuperekedwera kudzera m'ndondomeko yoperekera madandaulo.***
   - *Briefly discuss the advantages and disadvantages of each option. Focus on access (e.g., location, transportation, quality of staff and treatment of clients, cost of services, ability to influence service provision through complaints system/feedback).*
3. **Mukuganiza kuti ndi zifukwa ziti zikuluzikulu zomwe zimapangitsa anthu kusankha kukayezetsa HIV?**
   What do you think are the main reasons why people in your community choose to go for HIV testing?
   - ***Mukuganiza kuti ndi zifukwa ziti zikuluzikulu zomwe zimapangitsa azimayi/atsikana kupita kukayezesa HIV? Nanga azibambo/anyamata?***
     What about the main reasons why <u>women and girls</u> go for HIV testing? What about <u>men and boys</u>?
   - ***Kodi zifukwa zimene zatchulidwazi zimakhuza kuyezesa HIV kumene kumachitikira kulikonse/malo ena aliwonse, kapena zimangokhuza kuyezesa kumene kumachitika kumalo okhazikika oyezesera HIV monga kuchipatala, kapena kuyeza kumene kumachitika m'dera osati pa malo okhazikika ndi anthu oyeza HIV amene amayenda dera ndi dera?***
     Are these reasons specific to HIV testing in general, or facility-based testing only or mobile testing only?
4. **Mukuganiza kuti ndi zifukwa ziti zikuluzikulu zomwe zimapangitsa anthu kuti asapite kukayezetsa HIV?**
   What do you think are the main reasons why people in your community don't go for HIV testing in your community?
   - ***Kufuna kulipo koma anthu samapita chabe? Nthawi komanso kukana kuluza/kutaya zimena angapindule panthawi imene angawononge kupita kukayezesa? Kusafuna kuvomereza kuti ali pa chipsyezo? Kusaziwa njira yomwe angagwiritsire ntchito kuti apangange chiganizo ndi a bwenzi awo chokayezetsa limodzi? Mantha otsalidwa ndi anthu mmudzi mwawo, komanso nkhaza zomwe angakumane nazo? Kupanda chinsisi ndi kusowa chikhulupiliro pa anthu oyeza? Mmene anthu okayezesa amalandilidwira ndi anthu owathandiza akapita kokayezetsa? Ubale pakati pa anthu okayezetsa, komanso anthu oyeza?***
     Want to but just don't get around to it? Time and opportunity costs? Reluctance of individuals to acknowledge risk? Not knowing how to include their partner in the decision to test? Fear of stigma, discrimination & violence? Confidentiality & trust in service providers? Provider-client interactions (how users are treated)? Personal relationships between providers and clients?
   - **Mukuganiza kuti ndi zifukwa ziti zikuluzikulu zomwe zimalepheretsa azimayi/atsikana *kupita kukayezesa HIV? Nanga azibambo/anyamata?***
     What about the main reasons why <u>women and girls</u> don't go for HIV testing? What about <u>men and boys</u>?
     Kodi zifukwa zimene zatchulidwazi zimakhuza kuyezesa HIV kumene kumachitikira kulikonse/malo ena aliwonse, kapena zimangokhuza kuyezesa kumene kumachitika kumalo okhazikika oyezesera HIV monga kuchipatala, kapena kuyeza kumene kumachitika m'dera osati pa malo okhazikika ndi anthu oyeza HIV amene amayenda dera ndi dera?*Are these reasons specific to HIV testing in general, or facility-based testing only or mobile testing only?*

B. Perceptions of risk and health seeking

5. **Ndipazifukwa ziti/zokumana nazo zotani, (ngati mungathe kutchulapo), zomwe anthu akuyenera kupita ku kayezesa HIV, kapena kuyezetsa mowilikiza/kachikena.**

   Under what circumstances, if any, should people be testing for HIV or undergoing repeat testing?

   - ***Pazokhuzana ndi maubwenzi awo (mwachitsanzo, ngati chibwenzi chayamba kumene)? Malo Malo okuzungulira/amene munthu amapezeka pafupipafupi (e.g kuma bala), ntchito yomwe munthu amagwira (e.g., anthu oyendayenda/hule, anthu oyendetsa magalimoto akuluakulu-truck driver)? Zaka kapena kukhala wammuna kapena wamkazi?***
     Relationship circumstances (e.g. new vs. established relationships)? Environment circumstances (e.g. bars)? Occupational circumstances? (e.g., sex workers, truck drivers)? Gender or age (e.g. male or female, old or young)?

6. **Kodi kukhala munthu wa mmuna mudera lino, kumatanthauza chani? Kodi kukhala munthu wa mmuna kumakhuza bwanji mmene azibambo amasamalira umoyo wawo, makamaka, mokhuzana ndi HIV?**
   What do you think it means to be a man in this community? How does this affect the way that men take care of their health, particularly in relation to HIV?

   - ***Khalidwe lokhuza nkhani zo gonanana? Khalidwe lokhuza kufuna kulandira chithandizo cha zaumoyo, kapena chokhuzana ndi ku pewa HIV, Khalidwe lokhuzandi kuyezetsa kapena kulandila zithandizo zinazokhuzana ndi HIV, monga mankhwala a HIV?***
     Sexual behaviour? Access of health and HIV prevention, testing and care services?

7. **Kodi kukhala munthu wamkazi mudera lino kumatanthauza chani? Kodi kukhala munthu wamkazi kumakhuza bwanji mmene azimayi amasamalira umoyo wawo, makamaka, mokhuzana ndi HIV?**
   What do you think it means to be a woman in this community? How does this affect the way that women take care of their health, particularly in relation to HIV?

   - ***Khalidwe lokhuza nkhani zo gonanana? Khalidwe lokhuza kufuna kulandira chithandizo cha zaumoyo, kapena chokhuzana ndi ku pewa HIV, Khalidwe lokhuzandi kuyezetsa kapena kulandila zithandizo zinazokhuzana ndi HIV, monga mankhwala a HIV?***
     Sexual behaviour? Access of health and HIV prevention, testing and care services?

C. Distribution of HIV self-testing kits

8. **Ndi zinthu ziti zomwe mungawonesese kuti zizichitika mutati inu mukufuna kukhazikitsa njira yatsopano yoyezera HIV mdera lanu?**
   If you could choose to design a new service for HIV testing in your community, what are the components that you feel would be important to include?

   - ***Malo okayezetsera ndi mtengo woyezetsera? Mlingo wokuyakanirani nthawi yoyezesa? Ntchito yama khasala/anthu opereka uphungu? Mtundu/njira yoziyezera? Uthenga womwe uziperekedwa? Nkhani yokhuzana ndi kusungirana chinsinsi?***
   - *Location and cost? Level of supervision? Role of counsellors? Type of testing? Information provided? Issues surrounding confidentiality?*
   - **Kodi njira zimenezi zikhale chimodzimodzi kwa wina aliyense, kapena kuzikhala kusiyanisa pakati pa magulu a anthu osiyanasiyana, (e.g, azimayi vs azibambo, akulu vs achichamata)? Munjira yanji?**
     Should this be the same for everybody or should this differ to target different groups of people? (e.g., male vs female, old or young)? How?

9. **Kodi mukuganiza kuti anthu amudera lino angayiwone/angayitenge njira yoziyeza wekha HIV kukhala yobvomerezeka? Chifukwa chani angayiwone kuti ndiyobvomerezeka komaso ndi chifukwa chani angayitenge kukhala yosabvomerezeka?**
   Do you think people in this community would find self-testing acceptable? Why or why not?

   - ***Ndizinthu ziti zomwe zingafunike zitakhazikisidwa kuti njira yoziyeza wekha HIV ibweretsedwe mudera lanu?***
   - *What specific conditions would need to be in place in order to introduce self-testing in your community?*

10. **Ndondomeko yoziyeza wekha munthu yikayamba kupezeka mu madera anu, mukuganiza kuti anthu azizatha kupeza zipangizo zoziyezera motani?**
    When self-testing becomes available in your community, how do you think people should be able to access the self-test kits?

- **Ndi ndani amene akuyenera kumagawa zipangizo zoziyezera wekha mu madera anu? (e.g. Ntchito/udindo, wamkazi/wamwamuna, zaka) Kutiko komanso nthayi yanji yimene anthu azipeza zipangizo zoziyezera wekha? (e.g. Kunyumba, M'dera, malo ogulitsira mankhwala; Matsiku ongwira ntchito, matsiku opuma) Pakuyenera kukhala kulumikizana ndi malo opereka chithandizo cha za umoyo ngati zipatala zazing'ono, malo oyesesa HIV a VCT, anthu oyendera ndi kugwira ntchito za chipatala mu Madera/a phungu/malo oyezetserako magazi ndi kulandila uphungu?**
  Who should distribute self- test kits (e.g., occupation, sex, age)? Where and when should people be able to access self-test kits (e.g., home, community, pharmacy; weekdays, weekends)? What role/linkages should there be with health centres, VCT centres, HSAs, and counsellors?
- **Kodi njira zimenezi zikhale chimodzimodzi kwa wina aliyense, kapena kuzikhala kusiyanisa pakati pa magulu a anthu osiyanasiyana, (e.g, azimayi vs azibambo, akulu vs achichamata)? Munjira yanji?**
  Should this be the same for everybody or should this differ to target different groups of people? (e.g., male vs female, old or young)? How?

11. **Njira zoziyeza wekha HIV ikakhazikitsidwa mudera lanuli, ndi mlingo wanji wauthenga okhuzana ndi njira imeneyi mukuona ngati munthu akuyenera kulandira asanaziyeze yekha?**
    When self-testing becomes available in your community, what level of information do you think would need to be provided before someone self-tests?
    - ***Kodi uthenga umenewu uzikhala chimodzimodzi kwa wina aliyense, kapena kuzikhala kusiyanisa pakati pa magulu a anthu osiyanasiyana, (e.g, azimayi vs azibambo, akulu vs achichamata)? Munjira yanji?***
    - *Should this be the same for everybody or should this differ to target different groups of people? (e.g., male vs female, old or young)? How?*
12. **Njira zoziyeza wekha HIV ikakhazikitsidwa mudera lanuli, ndi mlingo wanji womwe munthu akuyenera kuyang'anidwira akamaziyeza kuti tionetsese kuti waziyeza mosatira ndondomeko yoyenera?**
    When self-testing becomes available in your community, what should be the level of supervision that is required to ensure that it is conducted properly?
    - ***Kodi kuyang'anidwira kumenewu uzikhala chimodzimodzi kwa wina aliyense, kapena kuzikhala kusiyanisa pakati pa magulu a anthu osiyanasiyana, (e.g, azimayi vs azibambo, akulu vs achichamata)? Munjira yanji?***
    - *Should this be the same for everybody or should this differ to target different groups of people? (e.g., male vs female, old or young)? How?*
13. **Njira zoziyeza wekha HIV ikakhazikitsidwa/kuyamba kupezeka mudera lanuli, kodi mukuona ngati anthu akuyenera kumutengara bwezi lawo/okondedwa wawo chipangizo choziyezera? Chifukwa chani akuyenera kumutengera, komanso ndichifukwa chani sakuyenera kumutengera?**
    When self-testing becomes available in your community, do you think people should be allowed to take a self-testing kit for their partner? Why or why not?
    - ***Kodi ddizophweka bwanji kuti azimayi ayambise nkhani yokhuza kuyezesa HIV komanso awapatse amuna awo chipangizo choziyezera HIV? Nanga ndizophweka bwanji kwa azibambo? Kodi kuphwekaku/kuvutaku zimatengera zifukwa zina zilizonse (Kuchuluka kwa nthawi imene anthu akhala paubwezi)?***
      How easy is it for women to bring up the topic of HIV testing and present a kit to their partner? How easy is it for men? Does this depend on other circumstances (e.g., length of relationship)?
    - ***Kodi ndi ubwino wanji kapena mavuto anji amene angabwere paubwenzi kamba kazimenezi?***
      What potential problems or benefits could this introduce into the relationship?

D. Characteristics of HIV self-testing kit

14. **Muli ndi maganizo otani pa chipangizo chimenechi?**
    What do you think of this test kit in general?
    - ***Kumvetsa malangizo ake? kumvetsa kawelengedwe ka zotsatira? kalongezedwe? kuphweka magwilitsidwe ntchito? Njira yoyeza magazi kapena njira yoyeza mkamwa?***
    - *Clarity of instructions? Clarity of reading results? Packaging of the kit? Presentation and user friendliness of the kit? Blood versus oral?*

15. **M'dera lanu lino, pali ubwino ndi kuyipa kotani poziyeza wekha kugwilitsa ntchito chipangizochi ngati chingakhazikitsidwe?**
    In this community, what do you think are the potential advantages and disadvantages of self-testing using this test kit?
16. **Kodi mutha kubvomera kulipira ndalama zingati kuti mupeze chipangizo chiziyezera atati chizigulisidwa? Chifukwa chani?**
    How much would you be willing to pay for this self-test kit? Why?
17. **Kodi pali kusiyana kotani pakati pa kuziyeza wekha ndi kupita kukayezetsa ku malo oyezera?**
    What do you think are the most important differences between self-testing and HTC?
18. **Kodi pali kusiyana kotani pakati pa kuziyeza wekha ndi kupita kukayezetsa ku malo oyezera?**
    What do you think are the most important differences between testing at home and testing at a facility?

E. HIV self-testing and counselling

19. **Njira zoziyeza wekha HIV ikakhazikitsidwa mudera lanuli, ndi uthenga wotani kapena uphungu wanji omwe munthu akuyenera kulandira akatha kuziyezayekha?**
    When self-testing becomes available in your community, what type of information or counselling, if any, should people receive after self-testing?
    - ***Kodi zimenezi zizikhala chimodzimodzi kwa wina aliyense, kapena kuzikhala kusiyanisa pakati pa magulu a anthu osiyanasiyana, (e.g, azimayi vs azibambo, akulu vs achichamata)? Munjira yanji?***
      Should this be the same for everybody or should this differ to target different groups of people? (e.g., male vs female, old or young)? How?
20. **Kodi mukuonangati uphungu kapena uthenga okhuzana ndi njira yoziyeza wekha uziperekedwa ndi ndani? Uthengawu/uphungu uziperekedwa banji (e.g ndi munthu, kapena pa phone)?**
    Who do you think should provide this information or counselling? How should this information or counselling be provided (e.g., in-person or telephone)?
    - ***Kodi zimenezi zizikhala chimodzimodzi kwa wina aliyense, kapena kuzikhala kusiyanisa pakati pa magulu a anthu osiyanasiyana, (e.g, azimayi vs azibambo, akulu vs achichamata)? Munjira yanji?***
      Should this be the same for everybody or should this differ to target different groups of people? (e.g., male vs female, old or young)? How?
    - ***Kodi tingawathandize bwanji anthu kuti akhonzekere kulandira zotsatira zawo, komanso kuvomereza zotsatira zakuziyeza kwawo?***
      What could be done to help prepare people for, or help them cope with, their self-test result?

F. HIV self-testing and linkage to care

21. **Njira zoziyeza wekha HIV ikakhazikitsidwa mudera lanuli, zingafunikire kupezeka ndizinthu ziti kuti munthu athandizidwe kuti akatsimikize zosatira zawo zitawonetsa kuti ali ndi kachirombo atatha kuziyeza, komanso kulumikizidwa ku chithandinzo choyenera?**
    When self-testing becomes available in your community, what would be needed to help people confirm their test if they received positive results after self-testing and link to support and care services?
    - ***Uthenga woperekedwa pamodzi ndi zipangizo zoziyezera pa pepala la malangizo otsatira po ziyeza wosonyeza kumene angapite? Nambala ya foni yopereka chithandizo chakomwe munthu akuyenera kupita? Kuimbilidwa phone ndi khasala, kuwathandiza kumvetsesa komwe angapite? Wachipatala kuwayendera pankhomo pawo kuti akawapase uphungu woperekedwa munthu akamaliza kuyezesa? Chithandizo choperekedwa munthu akaziyeza kukhala chokhazikitsidwa mudela lanu?***
      Information provided with the test kit on where to go? A help line number to call and ask where to go? A telephone call from a counsellor to help them to understand where to go? A home visit from a clinician to provide post-test services in the home? Post-test services made available locally in the community?
    - ***Kodi zimenezi zizikhala chimodzimodzi kwa wina aliyense, kapena kuzikhala kusiyanisa pakati pa magulu a anthu osiyanasiyana, (e.g, azimayi vs azibambo, akulu vs achichamata)? Munjira yanji?***
      Should this be the same for everybody or should this differ to target different groups of people? (e.g., male vs female, old or young)? How?

22. HIV self-testing and safety concerns

22. Ndiziopsyezo zanji zomwe mungamakumane nazo njira yakuziyeza wekha itati ya khazikitsidwa mudera lanu?

What safety concerns would you have if self-testing was made available in your community?

- ***Kuzipha? Kukakamizana kuti munthu ayezetse komanso aulule zotsatira zake? Nkhanza kwa azimayi/azibambo?***

  Suicide? Coercive testing or disclosure? Gender-based violence?

23. Ziopsyezo zimenezi, tingazikhonzekere motani, kuzichepesa kapenakuthana, nazo bwanji?

What would be the best way to anticipate and reduce the likelihood of these safety issues in this community?

Zikomo chifukwa cha nthawi yanu ndi kutengapo mbali mu kafukufukuyu. Taphunzirapo zambiri mukucheza kwathu lero ndipo tili ndi chikhulupiliro chakuti simunataye nthawi yanu pachabe.

Thank you for your time and participation. We have learnt a lot from our discussion here today and we hope the time has also been useful to you.